



Most Reverend George D. Tambala
Archbishop of Lilongwe

The Catholic Archdiocese of Lilongwe

Archbishop's House
P.O. Box 33, Lilongwe
Malawi - Central Africa

Telephone: (265) 01 754 667

Facsimile: (265) 01 753 045

Direct: (265) 01 754 674

Cell: (265) 994 244 345

Web email link: <http://lilongwearchdiocese.org>

E-mail: archbishop@lilongwearchdiocese.org

Our Ref: gdt/cal/circ/2026

9th September 2026

Kwa: Ansembe Onse, Asisteri, Ablazala, ndi Akristu Onse,

Okondedwa Abale ndi Alongo mwa Khristu,

KUKHAZIKITSIDWA KWA THUMBA LOKHALITSA LA TIYENDE LIMODZI ENDOWMENT FUND

Mtendere ukhale nanu m'dzina la Ambuye athu Yesu Khristu.

Ndikulemba kalatayi kuti ndithokoze kwambiri Ansembe onse, Asisteri, Ablazala, Akhristu eni ake kudzera ku Miphakati, mabungwe, onse akufuna kwa bwino ndi abwenzi a Arkidayosezi ya Lilongwe omwe munatengapo mbali kuti kukhazikitsidwa kwa **Tiyende Limodzi Endowment Fund, thumba lokhalitsa**, pa 25 July 2026 kuyende bwino, ndipo kuti kuyende mopambana. Mapemphero anu, kuwolowa manja kwanu, kudzipereka kwanu, ndi kutenga nawo mbali mwa khama pa Misa Yotsegulira ndi nkhomaliro ku Maula Cathedral, komanso pa phwando la madzulo (Legacy Gala Dinner), zasonyeza mgwirizano ndi kudzipereka kwa tonse ngati banja limodzi la Arkidayosezi yathu ino.

Ndikulimbikitsidwa kwambiri kuona kuti, kudzera mu mgwirizano wa anthu a Mulungu ndi anzathu ambiri akufuna kwa bwino omwe atithandiza, thumba limeneli linatha kusonkhanitsa **ndalama zoposa 300 miliyoni Kwacha mwa zopereka ndi malonjezo a zopereka**, kuposa momwe tinkayembekezera poyamba, ndipo izi zapereka maziko olimba okuti Thumba limeli likule ndi kupita patsogolo.

Kukhazikitsidwa kwa Tiyende Limodzi Endowment Fund, thumba lokhalitsa, ndi gawo lofunika kwambiri mu mbiri ya Arkidayosezi yathu ino. Thumbali latsegula njira yatsopano komanso yokhazikika yosonkhanitsira chuma chothandizira ntchito yomwe Yesu Khristu anatipatsa yofalitsa Uthenga wa Mulungu, ndikuwonetsetsa kuti anthu akulandira zithandizo zosiyanasiyana, pa maphunziro, pa za umoyo, ndi chitukuko cha munthu wina aliyense.

Kudzera mu kasamalidwe kabwino komanso kuyika ndalama m'njira zopindulitsa kwa nthawi yayitali, thumbali likufuna kulimbikitsa kuthekera kwa Arkidayosezi kuthandiza mibadwo ya lero ndi yam'tsogolo.

Phindu lomwe lidzakhale likupezeka lidzagwiritsidwa ntchito pa magawo anayi ofunika awa:

- **Ntchito za Uthenga Wabwino ndi Zaubusa (Pastoral Programming)**, kuphatikizapo chisamaliro ndi maphunziro a Ansembe athu ndi Asisteri, komanso Utumiki wa Akhristu eni ake;

- **Kayendetsedwe ka Arkidayosezi (Archdiocesan Operations)**, kuphatikizapo kayendetsedwe ka Archdiocese komanso kuthandiza mapulojeketi a m'maparishi;
- **Ntchito za Chitukuko cha Anthu (Social Development)**, kuphatikizapo Maphunziro, Zaumoyo ndi ntchito zina zachifundo kudzera mu Tiwale Limodzi Foundation; komanso
- **Ndalama zoyikidwa pa bizinesi ndi ntchito zopindulitsa za Arkidayosezi (Archdiocesan investments)**.

Ndine wokondwa kukudziwitsani kuti Tiyende Limodzi Endowment Fund yakhazikitsidwa ngati **bungwe lodziyimira palokha**, lovomerezeka ndi malamulo adziko, ndipo lalembedsedwa pansi pa mapepala ake aboma.

Bungweli lidzayendetsedwa motsatira ndondomeko zokulitsa ndi kuyang'anira chuma zomwe likukhazikitsa palokha, ndipo lidzakhala pansi pa utsogoleri wa **Board ya ma Trustees**, yomwe yakhazikitsidwa kuti ipereke utsogoleri ndi masomphenya, kuwonetsesa kuyankha pa udindo wake, komanso kusamalira bwino chuma chimene chaperekedwa ku Thumbali.

Ma Trustee omwe asankhidwa ndi awa:

1. Mr. Phillip Madinga – Wapampando
2. Ms. Beatrix Mosiwa – Wachiwiri kwa Wapampando
3. Bishop Vincent Mwakhwawa
4. Sr. Dorice Tembo
5. Mr. William Mwanza
6. Ms. Innocentia Ottober
7. Ms. Dziwana Shawa
8. Fr. John Kaliwamba
9. Mr. Hugo Mlewa

Board ya ma Trustees yandifotokozera kale njira imene ikufuna kutsatira polumikizana ndi Ansembe ndi Akhristu onse, monga anthu oyambilira komanso ofunikira kwambiri pa Thumbali limeneli. Ndikulandira ndi manja awiri lingaliro limeneli. Thumbali likufuna kusonkhanitsa **MK10 biliyoni** m'chaka chake choyamba kudzera mu zopereka za Akatolika, abwenzi athu omwe ali kunja kwa dziko, akufuna kwa bwino akumayiko osiyanasiyana, komanso mabungwe ndi makampani omwe ayamba kale kupeleka thandizo pa ntchito imeneyi.

Thumbali limeneli lidzakula pokhapokha ngati Akatolika tili ndi chikhulupiliro mwa ife, tikutenga nawo mbali, komanso tikuyiwona ngati thumba lathu lathu. Choncho, ndikofunika kuti aliyense mwa ife achite mbali yake ndipo Board ipitirize kugwira ntchito limodzi ndi magulu ndi maofesi onse a Mpingo pa magawo osiyanasiyana, kuti Thumbali likule motsatira kasamalidwe kabwino, moyankha poyera za kayendetsedwe, komanso mu njira yokhazikika ndithu.

Motero ndikupempha maparishi onse, ma deanery, magulu amu mpingo, mabungwe a Akhristu eni ake, Miphakati, komanso Mkhristu ndi mkatikumeni wina aliyense kuti agwirizane mokwanira ndi Board ya ma Trustees ndikuthandizira ntchito zake zolumikizana ndi anthu.

Pamene Board ikutifikira kuti ifotokozere zolinga ndi Thumbali, kukambirana nafe komanso kusonkhanitsa chuma, ndikukulimbikitsani kuti muwaladile bwino, mutenge nawo mbali mwakhama, komanso mupereke maganizo ndi chuma chomwe chingathandize kulimbikitsa Thumbali ndi kukwaniritsa cholinga chake.

Tiyeni tikumbukire kuti Tiyende Limodzi Endowment Fund si njira yosonkhanitsira ndalama chabe. Ndi chizindikiro cha kudzipereka kwathu pomanga Mpingo wodzidalira, umene utapitilize mwa mphamvu kulalikira Uthenga Wabwino ndi kutumikira anthu kudzera mu maphunziro, zaumoyo, ndi chitukuko cha anthu kwa ife ambadwo uno, komanso maka kwa mibadwo yambiri ya mtsogolo.

Pamene tikulowa m'gawo latsopanoli, ndikupempha kuti mupitirize kupempherera Board ya ma Trustees ndi onse amene adzatumikire Thumbali limeneli. Mzimu Woyera awatsogolere ndi kuwapatsa nzeru, kukhulupirika ndi luntha pa ntchitoyi, ndipo Ambuye adalitse onse amene athandiza kale komanso onse amene adzapitirize kuthandiza ntchito yabwinoyi m'miyezi ndi zaka zikubwerazi.

Ndine wanu mwa Khristu,



+Most. Rev. George Desmond Tambala, O.C.D
Archbishop of Lilongwe

